Maphunziro

a

Alangizi othandizira alimi a ziweto m'midzi

Mawu otsogolera

Small Scale Livestock and Livelihoods Program
PO Box 1604, Lilongwe Malawi

Mawu otsogolera

Dziko la Malawi limadalira kwambiri ulimi pa chuma ndiponso chakudya. Mu ulimi a Malawi amapeza chuma chimene chimathandiza kutukula miyoyo yawo akagulitsa mbewu kapena ziweto zawo. Kotero kuti kupereka ulangizi wamakono kwa alimi ndi ntchito yofunikira kwambiri papopititsa patsogolo kapezedwe ka chakudya ndiponso chuma m'dziko muno.

M'zaka zino, zaoneka kuti ulangizi pa ulimi waziweto watsika kwambiri malingana ndi kafukufuku amene a Sukulu ya Ukachenjede ya Bunda anachita mu chaka cha 2008 m'maboma a Kasungu ndi Mzimba. Zina mwazifukwa zimene zapangitsa, ndikuchepa kwa alangizi a ziweto m'dziko muno. Choncho njira imodzi yothandizira kuti ulimi wa ziweto ubwerere m'chimake ndi kukhala ndi alangizi aziweto akumidzi konko oti azithandizana ndi alangizi olembedwa ndi boma komanso mabungwe pantchito yopereka upangili pa ziweto. Ndondomeko imeneyi inayamba kale m'Malawi makamaka mzaka za 1990 komanso ikugwiritsidwanso ntchito m'maiko ena ndi ena.

Bungwe la SSLPP polemba bukuli lagwiritsa ntchito ukatswiri umene ulipo pa zaulimi waziweto m'dziko muno komanso pogwiritsa ntchito zina mwantchito zomwe zagwiridwa ndi mabungwe odziwika padziko lonse lapansi ngati la Food and Agriculture Organisation (FAO), the South Pacific Commission, ndinso Heifer International. Zambiri pa zimene zalembedwa m'bukuli zatengedwa mu zolemba za Unduna Wa Malimidwe makamaka dipatimenti ya ulimi wa ziweto (DAHLD) komanso dipatimenti yoyang'anira ulangizi (DAES). Bungwe la SSLPP likuyamikila koposa upangili ochokera ku madipatimenti awiriwa.

Bukuli lalembedwa ndi malingaliro oti lithandize alangizi akumidzi pa ziweto (CAHWs), amene akuyembekezeka kuthandizana ndi alangizi a ziweto olembedwa ndi boma m'Malawi muno. Ngakhale bukuli lalembedwa kuti lithandizire kwathu kuno, likhonzkugwiritsidwa ntchito ndi m'mayiko oyandikana nawo amene angakhalenso ndi ndondomeko ngati imeneyi

Bungwe la SSLPP lili ndi chikhulupiliro kuti ndi bukuli, ndondomeko yokhadzikitsa ulangizi wa ziweto wotsogoleredwa ndi alimi eniache udzatheka. Zimenezi zikatheka, ulimi wa ziweto udzapita patsogolo kamba kakuti pakali pano alimi ena safikilidwa ndi mauthenga abwino pa ziweto kamba kochepa alangizi.

Sute Mwakasungula
Executive Director

22 February 2011

Kuthokoza

Bukuli lalembedwa ndi chithandizo chochokera ku Bungwe la Flemish International Cooperation Agency (FICA) kudzera mu project ya FICA/FAO yotchedwa Support to Agriculture Extension Services yomwe ili m'maboma a Mzimba ndi Kasungu.

M'malo mwa bungwe la SSLPP Malawi ndikufuna kuthokoza mabungwe ndi anthu awa amene apangitsa kuti ntchito imeneyi itheke:

Bungwe la FICA kamba ka chithandizo cha ndalama

Depatiment yoyang'anira ulimi wa ziweto (DAHLD)

Depatiment yoyang'anira ulangizi (DAES)

Kasungu ADD

Mzuzu ADD, ndi

Bunda College of Agriculture

Zina mwa zithunzi zili m'bukuli zachokera m'buku "Manual for the Primary Animal Health Worker" lolembedwa ndi bungwe la Food and Agriculture Organisation of the United Nations (FAO) komanso a Kyeema Foundation.

Mwapadera tikuthokozanso anthu awa amene analiunikira bukuli kuti limveke bwino:

Mr P A N Gondwe, KADD
Dr O Bakili, Bunda
Mrs G T Mvula, LADD
Mr G Manjawira, SLADD
Mr K Ndindi, DAES
Mr A J Kaliati, CVL
Mr C L K Chiwayula, Otanthauzira
Mr B F Lwara, SSLPP
Mrs D Chitete, SSLPP
Mr C Luhanga, SSLPP
Mr Kalimalwayo Mwakasungula, SSLPP

Tikuyamikila chithandizo ndi upangili umene waperekedwa kufikira kuti bukuli lisindikizidwe. Bukuli lithandiza kupititsa patsogolo ulimi waziweto m'Malawi.

Pat Boland
Field Veterinary Officer, SSLPP

Editor

22 February 2011